**EXAMINATION NUMBER.: ____________________**

# CHIKALA ZONE EXAMINATION BOARD

## 2022 PRE-MOCK EXAMINATION

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Thursday, 24 February** **Subject number: P032**

**Time allowed: 2 h 15 mins**

**1:00 – 3:15 pm**

**Dzina lanu ____________________________________________________**

**Dzina la sukulu yanu ____________________________________________**

## Malangizo

1. **Onetsetsani kuti pepela ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi**

2. Pepela ili lili ndi magawo anayi**: Gawo A, B, C** ndi **D.**

3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.

4. Lembani nambala ya mayeso pamwamba pa tsamba lililonse.

5. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.

6. Lembani yankho la mu **Gawo A** pa pepala lomwe lili kumathero kwa mafunso a mu Gawoli.

7. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi C m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pafunso lililonse.

8. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza limbo lokhoza pa funso lililonse.

9. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funsolililonse lomwemwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikusogolo kwake.

10. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso **(imvijireta)** pepala lonseli nthawi ikakwana

| **Funso** | **Chongani Zomwe Mwayankha** | **Muno musalembemo** | |
|---|---|---|---|
| **1** | | | |
| **2** | | | |
| **3** | | | |
| **4** | | | |
| **5** | | | |
| **6 – 10** | | | |
| **11- 15** | | | |
| **16 - 20** | | | |
| **21- 25** | | | |
| **26 - 30** | | | |
| **31 - 35** | | | |
| **36 - 40** | | | |
| **41 - 45** | | | |
| | | | |

## **Gawo A** (Malikisi 30)

**Langizo:** yankhani funso **limodzi lokha** mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena wa kalata. Mawu a chimangirizo chanu **kapena** kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150.**

**1.** Lembani chimangilizo pa mutu wa

**MUDZI WA KWATHU**

Mwa zina tsatirani izi:

**Ndime yoyamba**

- Dzina la mudzi wanu
- Komwe mudziwo umapezeka
- Mudziwo wayandikana ndi chiyani?
- Mukuganiza kuti m'mudzimo muli anthu angati?

**Ndime yachiwiri**

- Ndi mbewu zanji zomwe zimalimidwa m'mudzimo?
- Nanga amakagulitsa kuti mbewuzo?
- Popita kumsika anthu m'mudzimo amayenda bwanji?

**Ndime yachitatu**

- Tchulani mitundu ya anthu yomwe ikupezeka m'mudzimo.
- Kodi anthu amamvera anyakwawa?
- Fotokozani ngati anthu a m'mudzimo amagwirizana

**KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa phungu wa nyumba ya malamulo woyimirira dera lanu, Bokosi 7340, m'boma lanu kuti akupempherereni ku boma msewu wa phula m'dera lanu. Mwa zina tsatirani izi:

**Ndime yoyamba**

- Dzina la msewu
- Kumene msewuwo umapita
- Kutalika kwa msewuwo

**Ndime yachiwiri**

- M'mene msewuwo ulili panopa
- Mavuto omwe akuchitika chifukwa cha msewuwo
- Zomwe boma lingachite pa vuto la msewuwo

**Ndime yachitatu**

- kuthandiza kwa msewuwo ukakonzedwa. (Pelekani mfundo zitatu)

**Tsamba loyankhilapo**

## Gawo B (20 malikisi)

### KUMVETSA NKHANI

**3.** Werengani nkhani yotsatilayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatilawa.

M'mudzi wa Tinkhani, mudali anyamata awiri. Mayina awo adali Mayingiso ndi chikondi. Iwowa adali anthanga imodzi ndipo adali pa ponda apa nane mpondepo. Anyamatawa amkasewera limodzi masewero osiyanasiyana. Ngakhale makolo awo sadali pa ubwenzi wotere padalibe mangawa ena aliwonse.
Tsiku lina mwachizolowezi, anyamatawa adapita kukasewera. Adayamba kuponyerana dzaye. Masewerowo atafika paindeinde aliyense adaiwala kuti dzaye ndi mwala womwe. Mwa tsoka Chikondi ataponya dzaye lija lidakagwera pa mwendo pa Mayingiso. Posakhalitsa mayingiso adapsa mtima. "Sungandipweteke chotere. Lero uwona." adatero Mayingiso."Pepa ambwana, kodi awa sadali masewero chabe? Inetu sindidachite dala ayi" adatero chikondi modzimvetsa chisoni. Nthawi yomweyo malingiso adaliponya khofu. Chikondi adalewa ngati mphaka. Adaponyanso chibakera mkulewanso. Chifukwa cha mphamvu zachibakera chija, Mayingiso adagwa nacho yekha. Mwatsoka adakagwera pachipanda ndipo chidamulasa pa tsaya.

Posakhalitsa Mayingiso adayamba kulira. M'mene amkatero mkuti mkulu wina samalani akudza poteropo. Mkuluyo atafika pafupi adamudzutsa koma adali atavulalala koopsa. "Iwe tafotokoza chomwe chatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke mnyanga?" Chikondi adafotokoza m'mene zidayendera. " Mnyamata iwe akunena mzakoyu nzoona?" adafunsa a Samalani. M'malo mofotokoza adakhala ngati amutsutsula pa chilonda ndipo adalira kwambiri kuti makolo ake amve.

Pakuti mwana sasowa make posakhalitsa A Namaliza adatulukira. Atangoona adayamba kukalipa nati, "Wachita izi awona chimene chidameta nkhanga mpala". Chifukwa cha mantha Chikondi adathamangira kwawo kukafotokozela makolo ake zomwe zidachitika. Mayi a Chikondi Adatulukira nawonso akulalata. "Ndimafuna iwe. Mwana wako wavulaza mwana wanga. Lero undidziwa kuti ndine Namaliza!! Posakhalitsa mkangano udakula.

Mayi a Chikondi adatengera nkhaniyi kwa mfumu chifukwa awiriwa adalephera kukhalirana pansi. Ngakhale mfumu idayesa kuwayanjanitsa, a Namaluza sadatheke. "mfumu muli apa mwana wanga akangofa winanso atsamira mkono."

Maanja awiriwa adayamba kukhala moopana. Anyamatawa sankachezanso ngati kale chifukwa choopa makolo awo.

**Tsopano yankhani mafunso otsatilawa pa m'mizere ili pansi pa funso lililonse.**

a. Tchulani mayina a anyamata awiri amene atchulidwa mnkhaniyi.

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

b. Ndi masewera amodzi ati omwe anyamatawa amachita?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

c. Kodi Chikondi adampepeselanji mzakeyu?

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

d. Nchifukwa chiyani Mayingiso adayankhula mawu woti “Sungandipweteke chotere”?

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

e. Perekani dzina la mkulu yemwe adadzutsa Mayingiso atagwa.

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

f. A Namaliza adadziwa bwanji kuti amkalirayo adali mwana wawo?

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

g. Ndani adalankhula mawu oti “Ndimafuna iwe.”

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

h. Pelekani matanthauzo awiri osiyana a mawu awa:

Chipanda ______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

i. Perekani matanthauzo azining’a izi:

i. Tsamila mkono ______________________________

ii. Tsutsula pachilonda ______________________________

iii. Anthanga imodzi ______________________________

**(Malikisi 3)**

j. Kodi chinameta nkhanga mpala m’mkhaniyi akutanthauzanji?

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

k. Perekani mutu wa nkhaniyi?

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

## **Gawo C** (malikisi 10)

Yankhani mafunso onse **awiri** m’gawoli.

**4.** Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatilawo.

Akhwasulani: Odi! Odi!

A Nyajere: Eeee! Tikuopeni nanga mwangotiyendera?

Akhwasulani Musaope kwambiri. Kaya amuna anu alipo?

A Nyajere: Ayi palibe momwe achokera m’mawa sanabwere.

Akhwasulani: Chabwino ndachita mwayi sindivutika ndi kuyenda popeza a Natembo ndi Abiti Msewu muli pompano. M'mawa kuli liwamba nachi chimanga chofiila mudzawapatse amuna anu.

A Nyajere: Zikomo kwambiri mawa tidzatsuka mkamwa. Nanga simutivinira lero?

**Mafunso**

i. Kodi ndi malonje anji omwe mwawelengawa?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

ii. Tchulani mayi yemwe adalonjelana ndi a Khwasulani pakhomo pake?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

iii. Nanga mawu awa akutanthauzanji?

a) Tidzatsuka mkamwa

______________________________________________

b) Liwamba

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

iv. Kodi chimanga chofiila chimatanthauza chiyani?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

**5. Kupanga ziganizo**

Lembani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. balamanthu

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

b. pa

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

c. chikaliwo

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

d. tumbwa

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

e. mbonaona

______________________________________________

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

## Gawo D (Malikisi 40)

Zungulizani lembo lokhoza (**A, B, C** kapena **D**) m'mafunso otsatirawa.

**Mafunso 6 mpaka 10.** Sankhani mitundu ya mawu amene atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatilazi

**6.** Iwo angoti duu.
A. mvekero C. mfuwu
B. dzina D. mperekezi

**7.** Atsibweni sanakhale nawo pa mlandu.
A. mlumikizi C. mlowam'malo
B. mperekezi D. muonjezi

**8.** Bamboo Kachimwe amaganiza mofatsa.
A. dzina C. mfotokozi
B. mneni D. muonjezi

**9.** Atsikana aja adasonkhana pa msika.
A. mlowam'malo C. mfotokozi
B. mlumikizi D. muonjezi

**10.** A Nyoni anabwera ndipo apita.
A. mperkezi C. mfuwu
B. mlumikizi D. mfotokozi

**Mafunso 11 mpaka 15.** Sankhani mawu amene akutsutsanam'matanthauzondi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatilazi

**11.** Ukhondo ndiwofunika kwambiri.
A. ulemu C. utchisi
B. usiwa D. ufulu

**12.** Mnyamata wavala malaya ake.
A. wachotsa C. wataya
B. waviika D. wavula

**13.** Makedzana kudali mitengo.
A. makono C. zilumika
B. kale D. lero

**14.** Wakuba akagwidwa amaona mavuto.
A. nzero C. chenjezo
B. zodamutu D. mwayi

**15.** Apongozi anu abwela kale.
A. mfumukazi C. amalume
B. atatavyala D. mkamwini

**Mafunso 16 mpaka 20.** Sankhani mtundu wa dzina lomwe liri ndi mzere kunsi kwake.

**16.** Chifundo wakhoza mayeso.
A. la mwinimwini
B. la chibale
C. lopanda mwinimwini
D. la chinthu chokhudzika

**17.** Mdipiti wa galimoto za mtsogoleri wa dziko zadutsa.
A. lopanda mwinimwini
B. la chinthu chokhudzika
C. la mwinimwini
D. la unyinji

**18.** Mfumu yathu yabwera.
A. lokhudzika
B. lopanda mwinimwini
C. launyinji
D. lachibale

**19.** Mphepo ikuomba kuchokera cha kumvuma.
A. lamwinimwini
B. la chinthu chosakhudzika
C. la chinthu chokhudzika
D. la unyinji

**20.** Pali mtunda wautali.
A. lopanda mwinimwini
B. la mwinimwini
C. la chinthu chokhudzika
D. la unyinji

**Mafunso 21 mpaka 26.** Sankhani msintho wa aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatilazi

**21.** Anawa adaleredwa bwino.
A. wochitidwa C. wochitirana
B. wochititsa D. wochititsitsa

**22.** Osewera onse amavara malaya ofanana.
A. wochititsa C. wobwerezabwereza
B. wotsutsa D. wochitidwa

**23.** Anthu ena amatolatola zinthu za eni.
A. wobwerezabwereza C. wochitirana
B. wochitira D. wonyazitsa

**24.** Penyetsetsa kuti uwone zenizeni.
A. wochititsa C. wochititsitsa
B. wochitidwa D. owonetsetsa

**25.** Atsikanawo amenyerana mwamuna.
A. wochititsa C. wobwerezabwereza
B. wochitidwa D. wochitirana

**Mafunso 26 mpaka 30.** Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi:

**26.** Kukana nsalu ya akulu n'kuviika.
A. kulola kugwira ntchito yotopetsa
B. kulola kugwira ntchito yopanda malipiro
C. kulola kuchita chinthu chifukwa cha manyazi
D. kulola kuchita chinthu chifukwa chokakamizidwa

**27.** Mlendo ndi mame.
A. alendo sakhala pansi akafika pakhomo
B. alendo sakhala kuchoka akafika pakhomo
C. alendo sakhala kunyowa akafika pakhomo
D. alendo sakhala kuuma akafika pakhomo

**28.** Kum'gwiritsa mzako mwala.
A. kuphwanya chipangano ndi mzako
B. kugwirizana ndi mzako
C. kusiya kupita kumalo
D. kunena bodza longozembetsa kuti upewe chilango

**29.** Kupulumukira mkamwa mwa mbuzi.
A. kusiya kupita ku malo
B. kunena bodza longozembetsa dala kuti upewe chilango
C. kuchenjera pakamwa kuti umubere munthu
D. kulankhula kwambiri kuti mlandu ukukomere

**30.** Zengerezu adalinda kwawukwawu.
A. pagulu sakambirapo nkhani yachinsisi
B. kulowa m'mavuto chifukwa chakunyozera.
C. kusowa woti umuuze zovuta zako chifukwa chosamva
D. kuchitira zinthu dala cholinga choputsitsa ena.

**Mafunso 31 mpaka 35.** Sankhani mitundu ya awonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatilazi

**31.** Malitera ndi wamwano zedi.
A. wamuyezo C. wamalo
B. wofunsa D. wamchitidwe

**32.** Iwo abwera madzulo.
A. wamuyezo C. wamafikidwe
B. wanthawi D. wowerenga

**33.** Nasibeko amayenda mofulumira.
A. wanthawi C. wamalo
B. wokulitsa D. wamchitidwe

**34.** Galu walowa m'nkhola la nkhuku.
A. wanthawi C. ofunsa
B. wamuyezo D. wamalo

**35.** Iyayi sindimudziwa
A. wamuyezo
B. wamalo
C. oyankha
D. wamchitidwe

**Mafunso 36 mpaka 40.** Sankhani matanthauzo oyenera a zilapi zotsatilazi.

**36.** Mfuti yanga yolasila kumbuyo.
A. tombotombo
B. njuchi
C. ntchetche
D. nthonga

**37.** Mbalame yaikira pa minga.
A. mutu
B. mano
C. lilime
D. maso

**38.** Muvi wa atate chibowola tsindwi.
A. utsi
B. mpaliro
C. lilime
D. mano

**39.** Nyama pamwamba chikumba mkati
A. chiwindi
B. chivululu
C. chikhadabo
D. mango

**40.** Amayi tsalani kumudzi ndipita ndi ine
A. chimanga
B. masamba
C. mapesi
D. mwana

**Mafunso 41 mpaka 45.** Sankhani mitundu ya nthambi ya chiganizo yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatilazi

**41.** Adatidziwitsa kuti aliyense ali ndi mwayi wopambana.
A. yoyima payokha
B. ya mfotokozi
C. ya dzina
D. ya muonjezi

**42.** Zoti adzapitanso kwawo ndi zonama.
A. ya muonjezi
B. ya dzina
C. yoima payokha
D. ya mfotokozi

**43.** Munthu amene amagulitsa mazira ndi wakuba.
A. yoima payokha
B. ya muonjezi
C. ya dzina
D. yamfotokozi

**44.** Bweretsani katunduyo ngati mukufuna chilungamo.
A. ya muonjezi
B. ya mfotokozi
C. ya dzina
D. yoima payokha

**45.** Ndaliya adalima mpaka dzuwa kulowa.
A. ya mfotokozi
B. yoyima payokha
C. ya dzina
D. ya muonjezi

**MAFUNSO ATHERA APA**

**NB: pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi.**